# Banja laling'ono, umoyo wathanzi mboma la Mchinji

## Banja la anthu ochepa limapindula mokwanila kuchokela ku zithandizo zosiyanasiyana za mdziko zokhudza miyoyo yawo.

- Mu zaka makumi awiri zapitazi chiwerengero cha anthu mu mzinda wa Mchinji chachulukitsidwa 4/5 kuchoka pa anthu 74 kufika pa anthu 136 pa $km^2$ ili yonse.
- Nyumba zokhala anthu zitatu (3) mwa nyumba zinayi (4) zili zones zili ndi potunga madzi a ukhondo pa makono.

**Nyumba zokhala anthu zisanu ndi zinayi (9) mwa nyumba khumi (10) zili zonse zimagwilitsa ntchito nkhuni pophika; ndipo nyumba imodzi (1) yokha mwa nyumba makumi awiri (20)zili ndi magetsi.**

**Amayi amodzi (1) okha mwa amayi khumi ndi zisanu ndi ziwiri (17) aliwonse; komanso abambo amodzi (1) mwa azibambo khumi ndi zisanu (15) aliwonse ndi amene amamaliza maphunziro awo a ku sekondale.**

- Amayi awiri (2) mwa amayi atatu (3) aliwonse komanso abambo anayi (4) mwa abambo asanu (5) aliwonse amadziwa kulemba, kuwelenga ndi kuwelengera.
- Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu ndi mmodzi (6) aliwonse komanso abambo amodzi (1) mwa abambo khumi ndi awiri (12) aliwonse sali pa ntchito iliyonse yolembedwa.
- Amayi anayi (4) mwa amayi asanu (5) aliwonse amavutika kwambiri kupeza chithandizo cha mankhwala akadwala chifukwa zipatala zoyandikila ndi kumene amakhala zili kutali kwambiri.

### Ubwino wotsatira njira za kulera

Banja likakhala ndi ana ochepa, zimathandiza makolo a anawa kuwaphunzitsa mokwanila ana awo ndipo chifukwa choti aphunzira bwino, anawa amakhala ndi mwayi wopeza ntchito zabwino mtsogolo. Kuchepetsa kachulukidwe ka anthu mdziko kumathandiza boma ndi mabungwe othandiza boma kukonzekera bwino pa ntchito zopititsa umoyo wa anthu patsogolo monga kukhala ndi madzi a ukhondo, ntchito za umoyo komanso za mtengatenga.

## Banja la anthu ochepa limakhala ndi mayi wa moyo wathanzi komanso banjalo limakhala losangalala

**Amayi amabeleka ana asanu ndi amodzi (6) pa moyo wao wonse koma amaonetsa chidwi chobeleka ana anayi (4) wokha pa moyo wao wonse.**

**Amayi amodzi (1) mwa amayi anayi (4) aliwonse a zaka za pakati pa khumi ndi zisanu (15) ndi zaka khumi ndi zisanu ndi zinayi (19) ayamba kale kubeleka ana.**

- Amayi amodzi (1) mwa amayi anayi (4) aliwonse amabelekela kunyumba osati kuchipatala.
- Amayi amodzi (1) mwa amayi awiri (2) aliwonse omwe ali pa banja amatsata njira za kulera; ndipo amayi amodzi (1) mwa amayi atatu (3) aliwonse amatsa njira zolererazi kuti asabeleke ana ambiri.
- Amayi amodzi (1) mwa amayi khumi ndi awiri (12) aliwonse komanso abambo amodzi (1) mwa abambo khumi ndi anayi (14) aliwonse amakhulupilira kuti ndi zovomelezeka kuti mamuna akhoza kumenya mkazi wake nthawi zina.

### Ubwino wotsatira njira za kulera

Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu ndi amodzi (6) aliwonse a zaka zapakati pa khumi ndi zasanu (15) ndi makumi anayi ndi zisanu ndi zinayi (49) amamwalira pa nthawi yobeleka mwana. Kutsatila njira za kulera kumathandiza amayi omwe ndi achichepeleko kutenga nthawi asanakhale ndi mimba (pathupi) ndipo kutenga nthaw chonchi kumathandiza kuti asapeze mavuto mthupi mwawo omwe amadza chifukwa chobeleka akadali ang'ono. Amayi ngati akhala ndi ufulu wosankha nthawi yoti abeleke komanso kusiyanitsa zaka za ana obelekedwa zimawathandiza kuti akhale ndi moyo wathanzi. Ana omwe amayi awo anamwalira nthawi zambiri samamaliza maphunziro awo ku sukulu.

## Banja la anthu ochepa ana ake amakula bwino komanso amakhala ndi moyo wathanzi


- Mwana mmodzi (1) mwa ana asanu ndi atatu (8) aliwonse wochepera zaka zisanu (5) amakhala ndi thupi lopelewela losagwilizana ndi msinkhu wawo.

**Mwana mmodzi (1) mwa ana awiri (2) aliwonse wochepera zaka zisanu (5) amakhala wopinimbira.**

### Ubwino wotsatira njira za kulera

Kutsatila njira za kulera kumathandiza ma banja kuti ana awo akule ndi moyo wathanzi komanso kutha kuonetsetsa kuti pakupita nthawi yokwanila bwino pamene mwana wabadwa ndi nthawi yomwe mwana wina akudzabadwanso mbanjamo. Ana obadwa mosiyana ndi zaka zitatu kapena kupitilira apo amakhala ndi mwayi wokhala moyo wochuluka kwambiri kuposa ana omwe abadwa mosiyana ndi zaka ziwiri kapena kuchepela apo. Makolo omwe ali ndi ana ochepa amasamalira bwino ana awo ndi kuwapatsa zakudya zokwanila.

Anthu awiri mwa anthu atatu aliwonse mbomali ali ndi zaka zosapitilira makumi awiri ndi zisanu (25)




**Source:** National Statistical Office of Malawi, *Population Projections Malawi.*

**Mdziko la Malawi, amayi amodzi amamwalira pobeleka ana pa ma ola awiri aliwonse.**

**Mwana wakhanda mmodzi (1) wosakwana chaka chimodzi amamwalira ma ola asanu ndi mmodzi (6) ndi ½ aliwonse.**

**Pa ma ola atatu (3) alionse mwana mmodzi wosakwanitsa zaka zisanu amamwalira.**


USAID FROM THE AMERICAN PEOPLE
IDEA INFORMING DECISIONMAKERS TO ACT
PRB INFORM EMPOWER ADVANCE
IPPF International Planned Parenthood Federation